

Maphunziro
a
Alangizi othandizira
alimi a ziweto m'midzi

Nkhuku

Small Scale Livestock and Livelihoods Program
PO Box 1604, Lilongwe Malawi



Nkhuku

Phunziro 1: Kuweta nkhuku za chikuda*

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. Kumvetsa za m'mene anthu amawetera nkhuku za chikuda m'Malawi muno
2. Kusiyanitsa mitundu ya nkhuku za chikuda zopezeka m'madera osiyanasiyana
3. Kufotokoza njira zosiyanasiyana za kawetedwe ka nkhuku za chikuda
4. Kufotokoza mitundu ina ya kawetedwe ka nkhuku zina kupatula za chikuda.

Yankhani mafunso awa:

Kodi ndi mitundu iti ya kawetedwe kankhuku yomwe imapezeka m'Malawi? Fanizirani ndi mitundu ya kawetedwe imene yalembedwa m'musiyi.

Fotokozani mabvuto omwe alimi amakumana nawo poweta nkhuku zachikuda. Lembani m'ndandanda wa mabvutowa kuyambira bvuto lalikulu zedi ndi kumatsika.

* (Dziwani izi: Zolembe izi ndi zolembera anthu akumudzi. Sizozama, ndipo zambiri zofotokoza kawetedwe kankhuku zanyama ndi zamazira mulibe. Ngati mufuna zambiri zakawetedwe kankhukuzi funsani ku bungwe loona za ziweto la SSLPP kapena kwa alangizi a za ziweto aku boma omwe muli nawo pafupi.

Mitundu ya kawetedwe ka nkhuu m'Malawi:

Zongotayira (Za m'mudzi)	Nkhuku zongotayira ndi zimene zikutchedwa za chikuda kapena za m'mudzi. Izi ndiye nkhuu zimene zimapezeka kuli konse m'Malawi muno. Izi zilipo zambiri kuposa zodyetsera/zowetera m'khola. Nkhuku zachikuda amazitsekura m'khola kuti zizikadya kunja kukacha ndipo sizipatsidwanso chakudya choonjezera chosakaniza. Amaziweta pofuna kupeza nyama ndi mazira ndi kuswanitsa.
Zodyetsera m'khola	Nkhuku zanyama (Broilers) amaziweta ndi cholinga chopeza nyama. Izi amazidyetsera m'khola ndi chakudya chochita kugula kapena chopangira pakhola pompo pophatikiza zakudya zoyenera zopezeka pakhomopo.
	Zamazira (Layers) amaweta pofuna kupeza mazira. Izinso amazidyetsera m'khola ndipo nthawi zina amaziika mtizipindazipinda; ndipo amazidyetsera chakudya chosakaniza ngati m'mene amachitira ndi zanyama.



Mitundu ya nkhuu zomwe zimawetedwa m'Malawi:

Mtundu	Ntchito yake
Mikolongwe (<i>Black Australorp</i>)	Zanyama ndi mazira
Zofiira (<i>Hyline</i>)	Zoikira mazira
Rose	Za nyama
Cobbs	Zanyama
Zoyela (<i>White leghorn</i>)	Zoikira mazira
Zachikuda	Mazira ang'onoang'ono ndi nyama

Mitundu ya nkhuu za chikuda

Yankhani mafunso awa:

Nenani mitundu ya nkhuu mwa maonekedwe ake zomwe zimawetedwa kumidzi m'Malawi muno. Lembani mitundu yonse yomwe mungathe kuiganizira. (Aliyense alembe mitundu ya nkhuu yomwe imapezeka m'dera la kwao). Fotokozani za mitundu ya nkhuu yomwe yalembedwa m'munsiyi.

Dzina	Maonekedwe ake	Kochokera dzinali
Kachibudu	Yopanda chitsukwa	Maonekedwe ake
Kameta	Yopanda nthenga mkhosi 	Maonekedwe ake
Masapa	Yokhala ndi nthenga ndi mzipalapasilo momwe	Maonekedwe ake
Kambwata/simboti	Kakafupi ndi miyendo yomwe 	Maonekedwe ake
Kansilanga	Nthenga zonyankhalala 	Maonekedwe ake
Tsumba	Yokhala ndi nthenga zatsumba pamutu	Maonekedwe ake
Kawanga	Yanthenga zamawangamawanga kufanana ndi kawando. (Mtundu wa nkhangha)	Mtundu
Chiphulusa	Mtundu wotuwa, yowoneka ngati phulusa	Mtundu
India	Inachokera ku India (yobwera)	Kochokera

Phunziro 2: Makola a nkhuu za chikuda (za kumudzi)

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:


- 1. Kumvetsa kufunika kwake kowetera nkhuu za m'mudzi m'khola labwino**
- 2. Kumvetsa zofunika kumangira khola ndi mamangidwe ake akhola la nkhuu za kumudzi**

Yankhani mafunso awa:

Fotokozani kufunika kwake komanga khola labwino la nkhuu zachikuda.

- Lembani zofunikirazi kuyambira ndi chofunikira zedi ndi kumatsika.
- Kodi ndi zithu ziti zimene zimapangitsa kuti aziti khola la nkhuu ili ndi labwino?
- Nanga ndi zipangizo ziti zimene zimagwiritsidwa ntchito pomanga khola la nkhuu za chikuda?
- Kodi makola ambiri a nkhuu zakumidzi sakhala abwino pazifukwa ziti?
- Fotokozani m'mene khola la nkhuu za kumudzi limakhalira molingana ndi: malo omangira, kukula kwake, pansi pake, zikopa zake, denga ndi malo okhala nkhuu

Mitundu ya makola a nkhuu yovomerezeka



Kasungidwe ka nkhuu kosaloledwa



Makola a nkhuu za kumudzi	
Cholinga	Kuteteza ku mvula, kutentha, kuzizira, kumphepo. Kuteteza kunyama zolusa monga amphaka, agalu, akalikongwe, anthu, afisi. Kuti nkhuu zizikhala mosangalala
Malo	Khola limangidwe pamalo pokwela osati podekha madzi Likhale pafupi ndi nyumba ya mlimi kuti azitha kuziteteza Likhale pamalo pouma Likhale pafupi ndi chitsime chotungapo madzi akumwa kuti madzi asamabvute
Kukula kwake	Kukula kwa pansi: nkhuu imodzi imafuna malo okwana muyeso wa phazi limodzi mbali zonse (30cm x 30cm) ndi malo ena ochepe osungira anapiye (Dziwani kuti apa tikunena zamalo ankhuku zomwe zimakhalira m'khola usiku okha. Koma malo okulirapo amafinikira kwa nkhuu zodyera m'khola.)
Pansi	Pansi pamakola ambiri pamakhala paubve. Pansi pothira simenti sipavuta kusamala. Pofuna kuteteza matenda, pansi pazikhala pouma nthawi zonse popeza pansi ponyowa pamaswanirana majeremusi oyambitsa matenda. Pansipa pakhalira pokwererapo ndi 20cm pogwiritsa ntchito timitengo ngati thandala la timipatatimipata kuti lizirola zitosi kumagwera pansi.
Zikupa	Zanjerwa zosaotcha, za njerwa zootcha, kapena mitengo ndi kuphoma/kumata Zikupa ziyenera kukhala zolimba ndithu pofuna kuteteza kumphepo yamkuntho. Koma ziyenera kukhala ndi timipata kuti mphepo izilowa bwino mkatimo. Mbali yaikulu yakhola ikhale ya mazenera okwanira kuti muzirowa mphepo yakwanira m'kholamo. Tiyenera kusiya malo oti munthu atha kumasesamo m'kholamo kuchotsa manyowa.
Denga	Denga lakhola lapansi likhale pazikupa zokwera ndi mikono iwiri (2 metres) kuchoka pansi ndipo likhale lofoleredwa mokwana kuti lisamadontha nthawi yamvula. Likhale lopitirira chikupa ndi 45 cm potchinjiriza ku mvula ya mpemera. Denga ndilofunika koma nthawi zina limapangitsa kuti m'khola muzitentha.

Makola a nkhuku za kumudzi	
Ndawala (Mitengo yokhalapo nkhuku m'khola)	Nkhuku zimafuna pokhala ndiye kuika mitengo yandawala m'khola ndibwino Mukhoza kugwiritsa ntchito mitengo kapena nsungwi za saizi ya bwino popanga ndawala (3-5cm kukula kwa tsinde) Ndawala zikhale zolimba ndi zomangidwa ku mphanda kapena miwati molimba. Nkhuku iliyonse imafuna mpata wa 20 cm okhalira pandawalapo. Ndawala zapamwamba zimangidwe mosemphanitsa kuti nkhuku zokwera pandawala zapamwambazo zisamanyerere zomwe zakhala pandawala zam'musizo

Phunziro 3: Kadyetsedwe ka nkhuu za kumudzi

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

- 1. Kumvetsa kadyetsedwe kosiyanasiyana ka nkhuu za kumudzi**
- 2. Kumvetsa za zakudya zofunikira kuthupi la nkhuu**
- 3. Kumvetsa za zakudya zomwe zimapezeka muzakudya zosiyanasiyana zimene amadyetsa nkhuu kumudzi**

Yankhani mafunso awa:

Fotokozani kuipa ndi ubwino wa kadyetsedwe ka nkhuu uku:

- Nkhuu zongotayira
- Nkhuu zongotayira ndi kumazipatsako chakudya
- Nkhuu zodyetsera zakudya zosakaniza magulu oyenera.

Kadyetsedwe	Ubwino wake	Kuipa kwake
Zongotayira	• Mlimi saononga ndalama • Mlimi satangwanika nazo • Sizifunika ukatswiri wina uli wonse	• Zimakhala zosamalika • Zimabvuta kusunga chiwerengero chofunika • Zimajiwa ndiponso kutenga matenda mosavuta
Zotayira ndi kumazipatsako chakudya	• Mlimi amaononga ndalama pang'ono • Amasamalako kadyetsedwe	• Chakudya chake sichikhala choyenera kwenikweni • Zimatangwanitsako pang'ono • Zimafunikira kudziwapo za zakudya zofunikira • Pamafunika ndalama zogulira zakudya • Zimajiwa ndiponso kutenga matenda

Zodyetsera m'khola ndi chakudya chosakaniza	• Zimapatsidwa chakudya chopatsa thanzi • Chakudya chamagulu malingana ndi msinkhu ndi mtundu wa nkhu: mwachitsanzo, zamazira. • Zimakula ndi kumaikira bwino • Sikukhala kobvuta kuteteza matenda • Zimatetezedwa	• Chakudya chimakhala chokwera mtengo • Khola limakhala lokwera mtengo pomanga • Chakudya chimapezeka mobvutira • Mlimi alibe ulamuliro pakasanizidwe kachakudya chomwe amagula pokhapokha asakanize yekha.
--	--	--

Nkhuku zotayira

- Nkhuku zotayira zimapeza zokha chakudya. Koma kupezeka kwa chakudya chofuna zokha kumatengera nyengo ya m'chaka, kumapeto kwa chirimwe, nkhuu sizipeza chakudya chokwana kusiyana ndi nyengo ya mwamvu. Pachifukwa ichi, ndi bwino kuwalimbikitsa eni nkhuu kuti azizipatsa chakudya choonjezera monga nkhuu, gaga/madeya ndi zina zotero maka nyengo ya chirimwe. Ngati achita izi, Ngati adzachita izi, mlimi adzapindula chifukwa nkhuu zimakula mofulumira ndi kuikira mazira ochuluka.
- Zakudya zina zoonjezera pa zakudya zomwe nkhuu zimapeza zokha ndi monga izi:
 - Zambiri zotsala za kukhitchini zomwe nkhuu zingathe kudya
 - madeya, misele ya mpunga ndi mbeu zina za mtundu umenewu
 - Inswa mbereswa, chiswe, nkhuu, nyongolotsi ndi tizilombo tina tokwawa ndi touluka
 - Chimanga, mpunga, mchewere, tirigu, mapira otsalira (**koma musazipatse nkhuu mbeu yothira mankhwala**)
 - Zotsala za kumunda monga lipoko, mbeu zina ndi zaudzu.
 - Masamba a mitengo monga a lukina, msangu kapena jerejere
 - Chiponde cha mbeu zopangira mafuta monga njere za thonje, ndi za mpenda dzuwa.
 - Ndi zina zomwe nkhuu zimadya.

Yankhani mafunso awa:

Fotokozani magulu azakudya amene amapangitsa kuti nkhuu zizikula bwino ndi kukhala zathanzi

Magulu azakudya

- Chopatsa mphamvu (Energy) (za ufa ndi mafuta) ndi zofunika pokulitsa. Ngati chakudya chiri ndi gulu la chakudya chopatsa mphamvu chochepa, ndiye nkhuu ziyenera kudya chochuluka. Ngati ziweto zidya chakudya chagulu lopatsa mphamvu chambiri, zimanenepa.
- Chukulitsa (Protein) chimakulitsa ndi kupangitsa chiweto chikhale ndi nyama yambiri ndi mazira ambiri.
- Mchere ndi zoteteza kumatenda: izi ndi zoti chiweto chizikhala chathanzi ndi mphamvu. Chakudya chosowa mchere chimapangitsa kuti anapiye akhale ofoka ndipo zikakhala zoikira mazira, mazira ake amakhala ndi zikokombe zofewa.
- Madzi: ndilo gawo lofunika zedi pamagulu onse azakudya. Madzi amapanga gawo lalikulu la thupi ngakhale dzira (70%- 85%). Madzi ndi chinthu chimene chimapangitsa kuti ntchito zambiri zochitika m'thupi la chamoyo zizichitika. Nkhuku zitha kukhala nthawi yaitali osadya, koma sizingakhalitse osamwa madzi. Madzi aukhondo ndi ofunika zedi. Onetsetsani kuti nkhuu zili kupatsidwa madzi aukhondo nthawi zonse.

Yankhani mafunso awa:

Tchulani zakudya zopatsa mphamvu? Zokulitsa? Zoteteza ku matenda?

Nanga nkuku zimapeza kuti gulu la za mchere?

- M'chimanga, mapira, mpunga, mchewere, chinangwa mbatata ndi mbewu zina za mtundu uwu ndiye zimapatsa mphamvu. Nkhuku zimakula zikamadyetsedwa zakudya zopangidwa kuchokera kumbewu zamtundu umenewu.
- Zakudya zonse za nkuku mumapezeka zagulu lopatsa mphamvu makamaka mwa zina zomwe zimapezeka m'Malawi muno ndi:
 - Mgaiwa, ndi madeya (gaga)
 - Mpunga, misere ya mpunga ndi gaga wake
 - Mapira ndi gaga wake
 - Chinangwa ndi mbatata
- Mwa zakudya zina momwe mumapezeka gulu lokulitsa ndi:
 - Nyemba, khobwe, soya, nandolo
 - Chiponde cha njere za thonje, chiponde cha mtedza (zochotsedwa mafuta)
 - Masamba a lukina ndi njere zophwanyanya za lukina
 - Nsomba, nyama ndi mafupa ogaya
 - Chiswe/ngumbi
- Gulu la mchere ndilofuka makamaka kwa anapiye ndi nkuku zoikira. Mchere wotchedwa calcium ndi wofunika pomanga mafupa ndi zikokombe za mazira. Pofuna kuonjezera mchere kuchakudya, tikhoza kuthirako mafupa a nyama kapena nsomba, zikokombe za mazira ngakhale zankhono, mutaziotcha ndi kuzipera bwinobwino.
- Zoteteza kumatenda ndi mchere zosakaniza kale zimapezeka kumasitolo amene amagulitsa mankhwala ndi zakudya za nkuku. Sikoyenera kupatsa nkuku zotayira mchere imeneyi chifukwa zimaupiza mchere umenewu kudothi ndi masamba amene zimadya kunja.

Phunziro 4: Matenda omwe amagwira nkhuku za kumudzi

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:


1. Kumvetsa za zizindikiro za matenda a nkhuku
2. Kumvetsa za zomwe zimayambitsa matenda a nkhuku za m'midzi kuno ku Malawi
3. Kudziwa njira zotetezera ndi kachiritsidwe ngati zilipo

Yankhani mafunso awa:

Lembani zizindikiro za matenda omwe amagwira nkhuku? Kodi chimayambitsa zizindikiro zimenezi ndi chiyani? Yerekezani zizindikiro zimene munalemba inuzo ndi zimene zalembedwa m'musizi:



Nkhuku ya thanzi



Nkhuku yodwala

Zizindikiro za matenda

- M'munsimu muli m'ndandanda wa zizindikiro za matenda omwe amakonda kugwira nkhuu ndi chomwe chingayambitse matendawo. Tiona tsatanetsatane wa nthenda iliyonse pasogolo.

Zizindikiro za matenda	Ndemanga
Kufooka, kuombwa, kuda kukhosi, kutseka maso, kuzyolika mutu, kunyankalala nthenga	Izi ndi zizindikiro za matenda ambiri ogwira nkhuu
Kutsokomola, kuyetsemula, kupuma mofulumira (befu), kutuluka mamina m'mphuno.	Izi ndi zizindikiro za mabvuto akapumidwe. China chake chalakwika ndi gawo la zakapumidwe. Pali matenda ambiri amene amayambitsa zizindikiro izi.
Mpwerere ndi chitosi cha mtundu wachilendo (chobiriwira, choyera, kapena chofira.), kosomera kokhala zitosi zokhazokha.	China chake chalakwika ndi gawo logayila zakudya. Mwina nkhuu zili ndi njoka zam'mimba, ndi mabakteria m'matumbo. Palinso matenda ambiri amene angaonetse zizindikiro zimenezi.
Kupinda khosi, kuyenda mwadzandizandi, kulephera kuyenda koyenera,	China chake chalakwika m'bongo ndi mitsempha (ma <i>nerve</i> .) Awa akhoza kukhala matenda a chideru kapena matenda ena oyambitsidwa ndi majeremusi (tizirombo tosaoneka ndi maso)
Kufa mwadzidzi	Pamene nkhuu zafa zambiri pamasiku ochepa apakati pa tsiku limodzi kufika asanu. Izi zikhoza kuchitika chifukwa cha matenda a chideru. <u>Izi zikachitika, muwauze alangizi mofulumira.</u>
Kufa miyendo ndi mapiko	Ndiye kuti china chake chalakwika ndi mitsempha (ma <i>nerve</i>). Awa akhoza kukhala matenda a chideru kapena matenda ena oyambitsidwa ndi majeremusi (tizirombo tosaoneka ndi maso.)
Kutupa mutu, lipombo ndi matende a nkhuu, ndipo amaoneka obiriwira.	China chake chalakwika ndi kayendedwe ka magari kumutu. Pali matenda ambiri oyambitsidwa ndi majeremusi amene angapangitse zizindikiro zimenezi.
Lipombo ndi matende zo oneka moyezuka	Kukhoza kukhala kuperewera kwa magari. Chifukwa choyambitsa chikhoza kukhala njoka za m'mimba zomwe zimamwa magari m'thupi la nkhuu.

Zizindikiro za matenda	Ndemanga
Totupa tokhala ngati zipere m'mutu ndi mozungulira m'amasomu	Akhoza kukhala matenda a chikwirikwiti. Nthawi zina totupa timeneti tikhoza kuyamba chifukwa cha nsabwe za nkuku, ndi tizirombo tina toluma.
Kukhota miyendo ndi kutupa molumikizira miyendo makamaka anapiye	Mafupa osalimba ndipo sangathe kunyamula thupi lankuku. Izi zitha kuyamba chifuwa chakuperewera kwa zakudya m'thupi.
Zotupatupa m'miyendo	Izi zitha kuyamba chifukwa cha nsabwe za nkuku ndi tizirombo tina toluma
Tizirombo takuda kuzungulira mzikope ndinso m'matende. (Nthata)	Iti tikhoza kukhala tinthata. Nthata izi zimasiyana ndi za agalu chifukwa izi siziyendayenda.



Yankhani mafunso awa:

Lembani m'ndandanda wa matenda a nkuku omwe amapezeka m'dera lanu.?

Perekani dzina lamatenda amene mwalembawo m'mene amadziwikira kuderalo ndi m'mene mungawatetezere ndi kuchiritsa kwake.

Matenda omwe amagwira nkhuku

- Tsopano tinena za matenda omwe amakonda kugwira nkhuku muno m'Malawi

Chideru 	 (Images courtesy of Cornell University College of Veterinary Medicine, Partners in Animal Health, and US Department of Agriculture, and Kyeema Foundation) Chideru chimagwa kawiri kapena katatu pachaka ndipo chimapha nkhuku zambiri pamasiku ochepa kapena pasabata.
Choyambitsa	Chideru chimayamba ndi kachirombo kakang'ono kwambiri kosaoneka ndi maso kotchedwa <i>virus</i> komwe kamafala ndi nkhuku kapena mbalame za m'thengo
Zizindikiro	Nkhuku zitha kumachita mpwerere, kupinda khosi, kuyenda mozungulira ndi kutuluka mamina kumphuno.
Kuteteza	Ngati nkhuku zalandira katemera moyenera sizingafe ndi matendawa atagwa m'deralo. Katemera wa chideru amateteza nkhuku ku matenda a chideru okha osati matenda ena. Nkhuku zomwe zalandira katemera wa chideru zitha kugwidwa ndi kufa ndi matenda ena.
Kuchiza	Palibe mankhwala ochizira matendawa. Koma atha kupewedwa pakutemera nkhuku basi.

Chifine cha nkhuu  Cornell University	  (Images courtesy of Cornell University College of Veterinary Medicine, Partners in Animal Health, and US Department of Agriculture) Matenda awa amapezeka kwambiri muno m'Malawi. Ndipo amafala kuchokera ku nkhuu zodwala pamene zakhala pafupi ndi zamoyo.
Choyambitsa	Kachiroambo kamtundu wa <i>bacteria</i> kamene kamapezeka kwambiri muno m'Malawi.
Zizindikiro	Matenda a chifine cha nkhuu amayamba mwadzidzidzi komanso angathe kuyamba pang'ono pang'ono. Matenda amenewa amagwira m'mpuno ndi malo ena amene amathandiza kupuma. Amatupitsa malo ozungulira m'maso ndi mutu wonse. Amayambitsa kutsokomola ndi chifine. Nkhuu zingathe kudwala matendawa kwa sabata limodzi kapena kupitililapo. Nkhuu zikhoza kufa ndi matendawa.
Kuteteza	Ndikosatheka kuteteza matendawa ku nkhuu zotayira. Ndikotheka kuteteza matendawa ku nkhuu zodyera m'khola poteteza nkhuu zina zodwala kubwera pafupi.
Kuchiza	Kuli mankhwala ochepa amene amachiza chifine cha nkhuu, makamaka mankhwala omwetsa.



Mthomba ya nkhuu (chikwirikwiti) 	 (Image courtesy of Cornell University College of Veterinary Medicine) Matenda awa amapezeka kwambiri muno m'Malawi. Ndipo amafala kuchokera ku nkhuu zodwala pamene zagundana ndi zamoyo.
Choyambitsa	Kachirombo kamtundu wa <i>virus</i> kamene kamapezeka kwambiri muno m'Malawi
Zizindikiro	Tizilonda totupa pa lipombo ndi m'matende. Nkhuku imadwala matendawa kwa sabata limodzi, nkhuu zina zitha kufa ndi matendawa.
Kuteteza	Pali katemera; koma sakonda kugwiritsidwa ntchito m'Malawi muno
Kuchiza	Palibe mankhwala ochiza matendawa. Ngati matenda agwa m'khola, amatha okha.

Njoka za m'mimba	Zimapezeka kwambiri mnkhuku za kumidzi. Njoka za m'mimba zimaikira timazira tating'onating'ono tomwe nkhuku imadyera limodzi ndi zakudya zomwe ikutola kunja. Timazirati timakagogomola ndi kusanduka njoka za m'mimba zazikulu zomwe zimayambanso kuikira mazira omwe amatulukira limodzi ndi zitosi.
Choyambitsa	Pali njoka za m'mimba zosiyanasiyana zomwe zimapezeka mnkhuku, pali zalaundi ndi zaphanthiphanthi
Zizindikiro	Kupinimbira, kutsika kwa kaikiridwe kamazira, mpwerere, kuombwa, ndi kufa.
Kuteteza	Ndikosatheka kuteteza njoka za m'mimba ku nkhuku zotayira chifukwa nkhuku zimatola mazira a njokazi zikamatola zakudya padothi. Ndikotheka kuteteza njoka za m'mimba ku nkhuku zodyera m'khola pozimwetsa mankhwala ophera njoka zam'mimba.
Kuchiza	Njoka za m'mimba zikhoza kuchizidwa ndi mankhwala omwetsa.

Nthata	Nthata zimagalika pochoka kunkhuku zina kupita kuzomwe zilibe ngati zikhalila limodzi.
Choyambitsa	Nthata zakhofi zomwe zimakangamira mzikope ndi mutu wa nkuku
Zizindikiro	Zizindikiro za kusowa kwa magari chifukwa nthata zimagamwa magari. Nkhuku siziikira mazira ambiri. Lipombo ndi matende a mayezuka chifukwa chakuchepa kwa magari ndipo nkuku zimafa ngati nthata zachuluka.
Kuteteza	Ndikobvuta kuteteza nthata chifukwa ana ake amakhalabe m'kholamo. Amayamba kudziphatika kunkhuku akakula. Wazani mankhwala nkuku zimene zaumbatira mazira.
Kuchiza	Nthata zikhoza kufa pozipaka mafuta a mtundu wagirizi (grease) chifukwa zimalephera kupuma. Mukhoza kupaka parafini, kapena Vaseline wodzola anthu uja. Koma mafutawa asapakidwe mbali yathupi yomwe kulibe nthata. Pakani mafutawa kangapo patsiku. Nthata zakufa sizigwa nthawi yomweyo koma pakapita masiku angapo.

Nsabwe za nkhuku za pakhungu	Nsabwe za nkhuku ndi mtundu wa nkhopakupa zomwe zimamwa magari ku nkhuku. Nsabwe zimenezi zimafala ndi nkhuku zobwera m'kholamo ngati zili ndi nsabwezi.
Choyambitsa	Ndi tizirombo tating'ona tomwe timabisara m'mang'alu a mchikupa masana. Usiku timatuluka ndi kumakaluma nkhuku ndi kuziyamwa magari.
Zizindikiro	Zizindikiro zimaoneka chifukwa magari amachepa m'thupi la nkhuku ndipo nkhuku zimamva kunyerenyesa. Lipombo ndi matende a mayezuka chifukwa chakuchepa kwa magari ndipo nkhuku zimafa ngati nsabwe zachuluka.
Kuteteza	Kusamalira m'khola kumachepetsa nsabwe. Makungwa a mitengo yogwiritsa ntchito pomanga khola achotsedwe kuti mungakhale mobisalira nsabwe.
Kuchiza	Pali mankhwala opopela kapena owaza ophera nsabwe. Mukhoza kufukiza utsi m'khola kuti nsabwe zimene zabisala m'mang'alu zife. Mukhoza kuwaza phulusa kapena laimu wothira kumbewu pansa ndi mzikupa kuti nsabwe zisowe kayendedwe.

Nsabwe zogwa m'miyendo ya nkhuku	Nsabwe zogwa m'miyendo ya nkhuku zimafala ndi nkhuku zomwe zili ndi nsabwezi zikagundana zomwe zilibe.
Choyambitsa	Kachirombo kakang'ono komwe kagwira mamba akuzipalapasilo ndipo zimatupa ndi kunyerenyesa.
Zizindikiro	Kutupa kwa khungu pazipalapasilo za nkhuku. Miyendo imatha kupunduka.
Kuteteza	Palibe njira zenizeni zotetezera.
Kuchiza	Nsabwe zikhoza kufa pozipaka mafuta a mtundu wagirizi (grease) chifukwa zimalaphera kupuma. Mukhoza kupaka parafini, kapena Vaseline wodzola uja. Koma mafutawa asapakidwe mbali yathupi yomwe kulibe nsabwe. Pakani mafutawa kangapo patsiku. Nsabwe zakufa sizigwa nthawi yomweyo koma pakapita masiku angapo. Pakani mankhwala kwa milungu itatu.

Chipumphu	  Chipumphu ndi matenda ogwira nkhuku omwe amafala ndi nkhuku zodwala matendawa. Nthawi zina nkhuku yomwe ikudwala matendawa imakhala yaikulu ndipo sionetsa zizindikiro zoti ikudwala. Chipumphu chimakonda kugwira nkhuku zomwe zimadyera m'khola ndi mwakamodzikamodzi chimagwira nkhuku zotayila.
Choyambitsa	Chipumphu chimayamba ndi kachirombo kakang'ono komwe kamaswana kwambiri m'matumbo ndi kuwaononga kwambiri. Kachilomboka kamapezeka mchitosi ndipo nkhuku imatenga kachilomboka ikamadya kuchokera pansu.
Zizindikiro	Nkhuku imachita mpwerere wosakanizika ndi magazi. Chipumphu chimakonda kugwira anapiye ndi nkhuku zomwe zikugona m'khola lonyowa. Chipumphu chitha kupha nkhuku.
Kuteteza	Nkhuku zisathinane m'khola ndipo onetesetsani kuti m'khola ndi mouma nthawi zonse.
Kuchiza	Alipo mankhwala ochiza chipumphu bola kuzipatsa mofulumira.

Matenda ena

- Alipo matenda ena omwe amapha ndi kudwalitsa nkhuku.
- **Perekani lipoti pamene nkhuku zikufa mwadzidzidzi:** Ngati muona kuti nkhuku zikufa zambiri kapena zikudwala, tumizani uthenga kwa alangizi a za ziweto msanga.

"Kufa mwadzidzidzi" ndi pamene nkhuku zafa zambiri pakanthawi/masiku ochepa - mwina pamene nkhuku zopitirira gawo limodzi la magulu anayi zifa pakati patsiku limodzi kufika masiku asanu.

Mafunso apomaliza pa maphunziro a gawo

1. Tchulani mitundu yosiyanasiyana ya nkhuku zachikuda zomwe zimapezka m'Malawi molingana ndi maonekedwe ake.
2. Kodi mukamanga khola zinthu izi amati zikhale motani?
 - Malo
 - Kukula kwa malo a nkhuku imodzi pansi
 - Malo a nkhuku imodzi pa ndawala (*perch*)
3. Tchulani magulu a chakudya chimene nkhuku imafuna.
4. Tchulani zina mwa zakudya zomwe zili m'gulu la zopatsa mphamvu zomwe amadyetsa nkhuku.
5. Tchulani zina mwa zakudya zomwe zili m'gulu lokulitsa zomwe amadyetsa nkhuku.
6. Tchulani zizindikiro zamatenda a nkhuku.
7. Kodi zizindikiro za matenda a chideru ndi ziti?
Nanga mankhwala ochizira chideru ndi chiyani?
Nanga njira yakatetezedwe ka chideru ku nkhuku ndi ziti?